Katekisimu wa Mbiri ya Baibulo
Nkhani za M'baibulo za Chipangano Chakale

NTHAWI YA KULENGEDWA KWA DZIKO MPAKA YA SAMUELI

Oyamba kumene (Kalasi yoyamba)
Buku loyamba la atatu

Lolembedwa ndi **Rev. C. Hanko**
Lakonzedwa ndi **Pastor J.J.Lim**
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** komanso **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

January 2011 edition

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Katekisimu wa mbiri ya M'baibulo- Nkhani za M'baibulo za Chipangano Chakale
(nthawi ya kulengedwa kwa dziko mpaka ya Samueli)
(Oyamba kumene Kuphunzira- Buku loyamba la atatu)

Lalembedwa ndi **Rev C.Hanko**
Lakonzedwa ndi **Rev. J.J.Lim**
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Buku leni leni loyambilira limene anatanthauzira ndi Rev C, Hanko eni ake ndi a Prostestant Reformed Churches of America
Buku ili lakonzedwanso ndi Rev. J.J. Lim mu 2011 mothandizidwa ndi Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media
Blk 203B, Henderson Road , # 07-07, Singapore 159546
Website: www.gdsmedia.org
Email: gdsmedia.sg@gmail.com

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa ntchito mu mipingo yawo yonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Mau oyambilira a Mlembi

Iri ndi gawo loyamba la mabuku atatu lomwe likufotokoza za mbiri ya Baibulo kwa ana a zaka 6 mpaka 8. Buku loyambali likufotokoza kuyambira chilengedwe cha dziko mpaka oweruza.

Phunziro lirilonse likufotokoza kachigawo kamodzi ka zochitika zofunika zokhazo. Aphunzitsi atha kuwona zina zomwe angawonjezere pokambirana koma kumbukirani kuti ana aang'ono amatchera khutu pa zinthu zochepa.

Atate a kumwamba adalitse mbewu ya chipanganoyi, kuti choona cha Mawu Ake chisungidwe mmitima mwawo ndi kupitilira ku mibadwo ina kuti Dzina lake lilemekezeke.

- Rev. C. Hanko

Mau oyambilira a mkonzi

Kugwiritsa ntchito Katekisimu pofuna kuphunzitsa ana aang'ono mu mpingo ndi njira yakale. Timabuku tino taknzedwa kuti tipereke chiyambi cha mbiri ya Baibulo kuti zikhale maziko a maphunzitso a katekisimu monga Katekisimu wachidule wa Westminister

Kabuku kano kakhala kakukonzedwanso patapezeka zolakwika zina mbuku lathu loyamba; Pastor David Higgs akhala akuwerenganso kuona zolakwika ndi kupereka maganizo awo. Mafunsonso akhala akukonzedwa (titamva maganizo a makolo) kuti kuloweza mayankho kukhale kosavuta kwa ana athu.

Talembanso kabuku kokhala ndi zochita. Tikulimbikitsa makolo kuti athandize ana awo kuchita zomwe ziri mkabukuka kuphatikizapo kuloweza pa mtima mayankho a mafunso 10 sabata iriyonse. Aphunzitsi a sabata sukulu ndi wongothandizira. Makolo, makamaka abambo afotokozere ana awo mwa njira yowayenera asanaphunzire mkalasi. Mkalasimo, aphunzitsi aphunzitse ana za moyo wawo watsiku ndi tsiku wa zomwe aphunzira ndi kubwerezanso phunziro ndi mwana aliyense ndi kuwayesa zomwe aloweza.

Yehova adalitse ntchito yophunzitsa anayi mwa njira yomwe Yehovayo afunira.

- Pastor J. J. Lim

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 1
CHILENGEDWE CHA DZIKO LA PANSI
Genesesi 1

1. Ndani adakulengani?
Mulungu. (Gen 1:27)

2. Kodi Milungu ilipo ingati?
Alipo Mulungu mmodzi woona. (Deut 6:4)

3. Kodi Mulungu adalenga zinthu zonse?
Inde, pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi pano. (Gen 1:1)

4. Tsiku loyamba Mulungu adalenga chiyani?
Kumwamba ndi dziko lapansi pano ndiponso kuwala. (Gen 1:1-5)

5. Tsiku lachiwiri Mulungu adalenga chiyani?
Mlengalenga. (Gen 1:6-8)

6. Tsiku lachitatu Mulungu adalenga chiyani?
Mtunda, udzu, mitengo ndi maluwa. (Gen 1:9-13)

7. Tsiku lachinayi Mulungu adalenga chiyani?
Dzuwa, mwezi, ndi nyenyezi. (Gen 1:14-19)

8. Tsiku lachisanu ndi chisanu ndi chimodzi, Mulungu adalenga chiyani?
Nsomba ndi mbalame, nyama ndi munthu. (Gen 1:20-31)

9. Tsiku lachisanu ndi chiwiri, Mulungu adachita chiyani?
Adapuma ndi kutipatsa ife tsiku la Sabata. (Gen 2:2)

10. Tidziwa bwanji za chilengedwe?
Mulungu akutiuza mMawu ake mBaibulo.

Vesi loloweza pamtima:
"Ndipo adaziona Mulungu zonse adazipanga, ndipo , tawonani zinali zabwino ndithu. "
(Gen 1:31)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 2
ADAMU MPARADIZO
Genesesi 1,2

1. **Makolo athu oyambilira ndiwo yani?**
   Adamu ndi Eva. (Gen 3:20)

2. **Mulungu adampanga adamu kuchokera kuti?**
   Kudothi. (Gen 2:7)

3. **Adamu ankasiyana bwanji ndi zinyama?**
   Mulungu adampanga mchifanizo chake. (Gen 1:26-27)

4. **Mulungu adawasiya adamu ndi Eva kuti?**
   Mmunda wokongola wotchedwa Eden. (Gen 2:8)

5. **Ndi mtengo wanji wapadera umene unali mmundamo?**
   Mtengo wa Moyo. (Gen 2:9)

6. **Ndi mtengo uti umene Adamu ndi Eva sadayenere kudya zipatso zake?**
   Zipatso za Mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa. (Gen 2:16-17)

7. **Adamu ankachita chiyani mmunda wa Edeni?**
   Ankasamalira mundawo ngati mfumu yake. (Gen 2:15)

8. **Adawonetsa bwanji kuti iye ndi mfumu?**
   Adapereka maina a nyama zonse. (Gen 2:20)

9. **Kodi Adamu ndi Eva anali wosangalala mmunda wa Edeni?**
   Inde, chifukwa ankatumikira Mulungu mwa chikondi. (onaninso monga Yes 51: 3)

10. **Munda wa Edeni ukufanizira chiyani?**
    Kumwamba komwe nkodabwitsa kwambiri. (onaninso monga Chi 22:1-2)

Vesi loloweza pamtima:
"Yehova, Ambuye wathu, Dzina lanu liposadi nanga padziko lonse lapansi!" (Mas 8:9)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 3
KUCHIMWA KWA ADAMU
Genesesi 3

1. Kodi adamu ndi Eva adakhalabe mmunda wa Edeni?
Ayi, Mulungu adawathamangitsa. (Gen 3:23-24)

2. M'chifukwa chiyani Mulungu adawathamangitsa mmunda wa Edeni?
Sadamvere Mulungu. (Gen 3:17, 22-24)

3. Adamu ndi Eva sadamvere Mulungu potani?
Adadya chipatso cha Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoipa. (Gen 3:6)

4. Chifukwa chiyani kunali kuchimwa kudya chipatso cha mtengowo?
Mulungu adawaletsa kutero. (Gen 2:16-17)

5. Ndani adanyenga eva kuti adye chipatso cha mtengowo?
Satana, woipayo, mngelo wokugwa. (Gen 3:1-5; onaninso 2 Pet 2:4)

6. Satana adadza bwanji kwa Eva?
Kudzera mwa njoka yomwe inalankhula ndi Eva (Gen 3:1-5 onaninso Chi 20:2)

7. Kodi Eva adamvera Satana?
Inde, adadya chipatso cha mtengo uja ndi kukapereka china kwa Adamu, nayenso nadya. (Gen 3:6)

8. Chidachitika nchiyani atakana kumvera Mulungu?
Ululu ndi chisoni zinadza padziko lapansi. (Gen 3:16-19)

9. Kodi nafenso tidafa mwa Adamu?
Inde, tonse tiri akufa muutchimo. (Aroma 5:12-21; 1 Ako 15:22)

10. Adamu atagwa, Mulungu adamulonjeza chiyani?
Mpulumutsi, kudzatipulumutsa ku machimo athu. (Gen 3:15)

Vesi loloweza pa mtima:
"Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yake; idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira chitende chake." (Gen 3:15)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 4
KAINI APHA M'BALE WAKE
Genesesi 4

1. Ana awiri a Adamu ndi Eva ndiwo ati?
Kaini ndi Abele. (Gen 4:1-2)

2. Baibulo litiuzanji za Abele?
Abele ankaopa Mulungu. (Mat 23:35; Ahe 11:4)

3. Abele anachita chiyani poonetsa kuti ankaopa Mulungu?
Anapereka nsembe ya mwana wa nkhosa kwa Mulungu. (Gen 4:4)

4. Chifukwa chiyani izi zinamusangalatsa Mulungu?
Chifukwa Abele anakhulupilira Kankhosa ka Mulungu. (Ahe 11:4; onaninso Yoh 1:36)

5. Baibulo litiuza zotani za Kaini?
Kaini anali ochimwa. (Gen 4:9-10; onaninso 1 Yoh 3:12)

6. Kaini anaonetsa bwanji kuyipa kwake?
Anapereka nsembe yopanda magazi. (Gen 4:3)

7. Chifukwa chiyani ili linali tchimo?
Zisonyeza kuti sanamve chisoni ndi machimo ake? (Gen 4:6-7; onaninso Ahe 13:11-12; 1 Yoh 1:7)

8. Kaini anaonetsanso bwanji kuchimwa kwake?
Anachita nsanje ndi Abele ndi kumupha. (Gen 4:8)

9. Mulungu anamulanga bwanji Kaini atachimwa?
Anamuthamuthamangitsa iye ndi banja lake. (Gen 4:11-12, 16)

10. Kodi Mulungu adampatsa mwana wina mmalo mwa Abele?
Inde, anampatsa Seti, mwana woopa Mulungu. (Gen 4:25)

Vesi loloweza pa mtima:
"Ndi chikhulupiliro, Abeli anapereka kwa Mulungu nsembe yoposa ija ya Kaini" (Ahe 11:4)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 5
CHIGUMULA CHISANAFIKE
Genesesi 4:17 – 5:32

1. Kaini atapha mbale wake Abele, zitiuzanji?
Anachimwirachimwirabe, komanso anaphunzitsa ana ake kuchimwa. (Gen 4:17-24)

2. Mwana woipa wa Kaini ndiye yani?
Lameki, wachifwamba ngati bambo wake. (Gen 4:23-24)

3. Ana oipa a Lameki adachita chiyani?
Ankaweta ng'ombe, ankayimba zeze, zitoliro, komanso anali amisiri a zinthu za mkuwa ndi chitsulo. (Gen 4:20-22)

4. Kodi adagwiritsa ntchito zidazi pochimwira?
Inde, adachimwirachimwira. (Gen 6:5)

5. Baibulo litiuzanji za ana a Seti?
Amakumana pamodzi kupembedza Mulungu. (Gen 4:26)

6.Ndi munthu uti woopa Mulungu anakhalapo nthawi imeneyi?
Enoki amene ankayenda ndi Mulungu. (Gen 5:24)

7. Mulungu adamuuza chiyani Enoki?
Alalike za anthu oyipa. (Yud 14)

8. Enoki adauza anthu oyipawo kuti chiyani?
Mulungu adzawalanga. (Yud 15)

9. Adamumvera Enoki?
Ayi, adafuna kumupha. (Yud 16; onaninso Mat 23:37; 2 Tim 3:12)

10. Adamupha Enoki?
Ayi, Mulungu adamutenga kupita naye kumwamba. (Gen 5:24)

Vesi loloweza pamtima:
"Ndipo Enoki anayendabe ndi Mulungu; ndipo panalibe iye; pakuti Mulungu anamtenga." (Gen 5:24)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 6
CHIGUMULA
Genesis 6 - 9

1. Baibulo litiuzanji za Nowa?
Anali mmodzi mwa anthu ochepa amene ankaopa Mulungu. (Gen 6: 8-9; 7:1)

2. Mulungu adamuuza Nowa kuti achite chiyani?
Apange chombo. (Gen 6:14)

3. Ndi chifukwa chiyani Nowa adayenera kupanga chombo?
Mulungu ankafuna kutumiza chigumula. (Gen 6:13, 17)

4. Nowa ndi ana ake anatha nthawi yotalika bwanji kupanga chombo?
Pafupi zaka 120. (Gen 6:3)

5. Nowa anachita chiyani pamene ankapanga chombo?
Analalika za Khristu ndikuuza anthu oyipawo kuti alape,akapanda kutero Mulungu adzawalanga. (1 Pet 3:18-20; onaninso 2 Pet 2:5)

6. Ndani adapulumuka mchombo muja?
Nowa ndi a mbanja mwake. (Gen 7:23; 8:16)

7. Ndi chiyaninso chinapulumuka mchombo muja?
Nyama zomwe Mulungu anazibwaretsa kwa Nowa. (Gen 8:16-17)

8. Chinachitika ndi chiyani kwa anthu oyipa aja?
Onse anawonongedwa ndi chigumula. (Gen 7:23)

9. Chigumula ndi chizindikiro cha chiyani?
Kutha kwa dziko la pansi. (Mat 24:37-39)

10. Kodi chizindikiro cha utawaleza chitanthauzanji?
Mulungu adzakumbukira ndi kupulumutsa anyhu ake. (Gen 9:9-17)

Vesi loloweza pamtima:
"Koma Nowa anapeza ufulu pamaso pa Yehova." (Gen 6:8)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 7
CHITATHA CHIGUMULA
Genesesi 9 - 11

1. Perekani maina a ana a Nowa.
Shemu, Hamu, ndi Yafeti. (Gen 5:32; 6:10)

2. Baibulo litiuzanji za Hamu?
Adanyoza atate ake. (Gen 9:22)

3. Nowa adati chiyani za tchimo la Hamu?
Adati mwana wa Hamu adzakhala wotembererdwa. (Gen 9:25)

4. Nanga za Shemu Nowa adati chiyani?
Mulungu adzakhala Mulungu wa Shemu. (Gen 9:26)

5. Ndipo zokhuza Yafeti Nowa adati chiyani?
Adati adzagawana madalitso ndi Shemu. (Gen 9:27)

6. Tchulani dzina la chidzukulu chimodzi cha Hamu.
Nimrode, woyipa kwambiri, komanso anali mlenje wamphamvu. (Gen 10:6-9)

7. Kodi anthu a nthawi imeneyi adachimwanji?
Anayamba kumanga mudzi ndi nsanja. (Gen 11:3-4)

8. Chifukwa chiyani anafuna kumanga mudzi ndi nsanja?
Anafuna kuti atchuke komanso asabalalike. (Gen 11:4)

9. Adaitsiriza nsanjayo?
Ayi, Mulungu adawasintha zilankhulo. (Gen 11:5-7)

10. Kenaka chinachitika nchiyani?
Anabalalika pa dziko lonse lapansi. (Gen 11:8-9)

Vesi loloweza pamtima:
"Yehova asunga onse akukondana naye; koma oyipa onse adzawaononga." (Mas 145:20)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 8
YOBU
Buku la Yobu 1 - 2, 19, 42

1. Baibulo litiuzanji za Yobu?
Yobu ankaopa Mulungu. (Yob 1:1, 8; 2:3)

2. Kodi Mulungu adamudalitsa Yobu?
Inde; Mulungu adampatsa ana khumi ndi ng'ombe zambiri. (Yob 1:2-3)

3. Satana anafuna kutani naye Yobu?
Anafuna kuti Yobu atemberere Mulungu. (Yob 1:9-11)

4. Satana adachitanji kuti izi zitheke?
Adamulanda ana ndi chuma chake chonse. (Yob 1:9-11)

5. Kodi Mulungu adalola kuti satana amuzunze Yobu?
Inde; ana onse ndi chuma chake chonse zidatha tsiku limodzi. (Yob 1:12-21)

6. Kodi Yobu adazunzikabe?
Inde; anadwala kwambiri. (Yob 2:4-8)

7. Yobu akuzunzika, kodi anzake atatu adamuthandiza?
Ayi; anangomuonjezera mavuto ake. (Yob 2:11; onaninso Yob 42:7-8)

8. Yobu anawayankha kuti chiyani?
Anati, "Ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi moyo." (Yob 19:25)

9. Akuzunzika choncho, Yobu anakhala motani?
Anali wodekha mtima. (Yak 5:11)

10. Kodi Mulungu adamdalitsa Yobu chifukwa cha kudekha mtima kwake?
Inde; Mulungu adachulukitsa kawiri chuma chake chonse, adampatsanso ana ena khumi. (Yob 42:10, 12-13)

Vesi loloweza pamtima:
"Yehova anapatsa, Yehova watenga, lidalitsike dzina la Yehova." (Yob 1:21)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 9
ABRAHAMU APITA KU KANANI
Genesesi 12-15

1. Kodi Mulungu adamuuza Abrahamu kuti achitenji?
Apite ku dziko limene Mulunguyo adzamusonyeze. (Gen 12:1)

2. Abrahamu ndi Sara adapita kuti?
Ku dziko la Kanani. (Gen 12:5)

3. Mulungu adamulonjeza chiyani Abrahamu?
Adzapereka dziko lonselo kwa ana ndi zidzukulu zake. (Gen 12:7; 13:14-15)

4. Dziko la Kanani linkafanizira chiyani?
Kumwamba. (Ahe 11:8-10, 13-16)

5. Mulungu adamulonjezanso chiyani Abrahamu?
Ana ochuluka ngati nyenyezi za kumwamba. (Gen 13:16; 15:5; 22:16-18)

6. Kodi Abrahamu ndi Sara anali ndi ana panthawiyi?
Ayi; komanso anali atakalamba. (Gen 15:2-4; onaninso Gen 17:15-17)

7. Chifukwa chiyani Abrahamu adapita ku Eguputo?
M'dziko la Kanani kudali njala. (Gen 12:10)

8. Kodi Mulungu adafuna kuti Abrahamu apite ku Eguputo?
Ayi, Mulungu adambwezera ku kanani, kuti adzikamusamalira komweko. (Gen 12:17–13:3)

9. Abrahamu adadziwa bwanji kuti Mulungu adzamdalitsa?
Mulungu adamuuza kuti. "Usaope, Abramu, ine ndine chikopa chako ndi mphoto yako yaikurukuru. (Gen 15:1)

10. Abrahamu adakhulupilira kuti Mulungu amudalitsa?
Inde; anakhulupilira Mulungu. (Gen 15:6)

Vesi loloweza pamtima:
"Pakuti analindilira mudzi wokhala nawo maziko , mmisiri wake ndi womanga wake ndi Mulungu." (Ahe 11:10)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 10
LOTI APULUMUKA KU SODOMU
Genesesi 13, 19

1. Abrahamu anapita ndi yani ku Kanani?
Mdzukulu wake, Loti, ndi mkazi wake. (Gen 13:1)

2. Chifukwa chiyani Abrahamu ndi Loti anasiyana?
Kunalibe msipu wokwanira wa ng'ombe zawo. (Gen 13:5-9)

3. Loti adakakhala kuti?
Pafupi ndi midzi ya anthu oyipa ndi ochimwa ya Sodomu ndi Gomora. (Gen 13:10-13)

4. Loti anali wosangalala ku Sodomu?
Ayi; koma banja lake linkasangalala kumeneko. (Gen 19:7, 14-16; onaninso 2 Pet 2:6-8)

5. Mulungu adamuuzanji Abrahamu za Sodomu?
Kuti Mulungu adzaononga mudzi woipawo. (Gen 18:16-32)

6. Kodi Abrahamu adapempherera Sodomu?
Ayi; anapempherera Loti yekha amene ankaopa Mulungu. (Gen 19:27-29)

7. Kodi Mulungu adampulumutsa Loti?
Inde; angelo awiri adapulumutsa Loti ndi banja lake mmudzimo. (Gen 19:1-17)

8. Mkazi wa Loti adawona zotani?
Anasanduka chulu cha mchere. (Gen 19:26)

9. Midzi imeneyi idawona zotani?
Mulungu anavumbitsa moto ndi sulfure kuchokera kumwamba. (Gen 19:24-25, 28-29)

10. Chiwonongeko cha Sodomu ndi Gomora ndi chizindikiro cha chiyani?
Kutha kwa dziko la pansi. (Mat 10:15)

Vesi loloweza pamtima:
"Tawonani, ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ndiri nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yake." (Chi 22:12)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 11
ISAKI
Genesesi 18, 21, 22

1. **Chifukwa chiyani Mulungu anamuyendera Abrahamu?**
   Kudzamuuza kuti Sara adzakhala ndi mwana, Isaki. (Gen 18:10)

2. **Chifukwa chiyani Sara adaseka pamene Mulungu adamuuza kuti adzakhala ndi mwana?**
   Chifukwa anali atakalamba kale. (Gen 18: 11-12)

3. **Mulungu adamuyankha Sara kuti chiyani?**
   Kodi chilipo chomulaka Yehova? (Gen 18:14}

4. **Ndani adamunyoza Isaki?**
   Isimaeli, mwana wa Hagara. (Gen 21:8-9)

5. **Kodi Mulungu adakwiya naye Isimaeli?**
   Inde; adamuuza Abrahamu kuti amuthamangitse Isimaeli ndi Hagara. (Gen 21:10-12)

6. **Mulungu adalamula Abrahamu kuti achite naye chiyani Isaki?**
   Ampereke nsembe kwa Mulungu. (Gen 22:2)

7. **Mulungu adauza Abrahamu kuti akampereke Isaki nsembe kuti?**
   ku phiri la Moriya ku yerusalemu. (Gen 22:2-4; onaninso 2 Mbi 3:1)

8. **Chifukwa chiyani Abrahamu adavomera kukampereka mwana wake nsembe?**
   Adadziwa kuti Mulungu adzamuukitsa mwana wake kwa akufa. (Ahe 11:17-19)

9. **Mmalo mwa Isaki, Mulungu adampatsa chiyani?**
   Nkhosa ya mphongo yomwe inali atakodwa mziyangoyango. (Gen 22:12-13)

10. **Kodi nkhosayi ikuimilira ndani?**
    Ambuye Yesu Khristu, Kankhosa ka Mulungu. (Gen 22:8; onaninso Yoh 1:29)

Vesi loloweza pamtima:
"Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi." (Yoh 1:29)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 12
YAKOBO
Genesesi 24-28

1. **Chifukwa chiyani Abrahamu anatuma mnyamata wake ku Harani?**
   Kukapeza mkazi wa Isaki. (Gen 24: 2-4)

2. **Chifukwa chiyani adapita ku Harani kukapeza mkazi?**
   Isaki sanayenera kukwatira mkazi wa mdziko lachilendolo. (Gen 24:3)

3. **Mnyamata wa Abrahamu adapeza bwanji mkazi?**
   Adapemphera kwa Mulungu kuti amuthandize kupeza mkaziyo. (Gen 24: 12-14)

4. **Ndani adakhala mkazi wa Isaki?**
   Rabeka. (Gen 24: 50-51, 67)

5. **Isaki ndi Rabeka adabala ana angati?**
   Mulungu adawapatsa ana amapasa, Yakobe ndi Esau. (Gen 25:24-26)

6. **Mulungu adamuuzanji Rabeka anawa asanabadwe?**
   Ankakonda Yakobo ndi kudana ndi Esau. (Gen 25:23)

7. **Esau adawonetsa bwanji kuti anali oyipa?**
   Anagulitsa ukulu wake ndi mbale ya nyemba. (Gen 25:29-34)

8. **Kodi Yakobo adapempha madalitso kwa atate wake molondola?**
   Ayi; adanamiza bambo wake. (Gen 27:18-19, 24)

9. **Yakobo adanyenga bwanji bambo wake?**
   Pomunamiza kuti anali Esau. (Gen 27:6-27)

10. **Chidachitika nchiyani pamene Esau adafuna kupha Yakobo?**
    Yakobo adathawira kwa Labani malume wake. (Gen 27:42-43; onaninso 28:10)

Vesi loloweza pamtima:
"Ndi chikhulupiliro, Isaki adadalitsa Yakobo ndi Esau, zingakhale za zinthu ziri nkudza." (Aheb 11:20)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 13
YAKOBO KU HARANI
Genesis 28-33, 35

1. Yakobo adakomana ndi zotani paulendo wopita ku Harani?
Mulungu adamuonekera mmaloto. (Gen 28:11-12)

2. Mulungu adamulonjeza chiyani mmalotomo?
Mulungu adzakhala naye ndi kumdalitsa. (Gen 28:13-15)

3. Yakobo adakhala ndi Labani zaka zingati?
Zaka 20 akutumikira akazi ake ndi ng'ombe zawo. (Gen 31:38, 41)

4. Yakobo anali ndi akazi angati?
Awiri: Leya ndi Rakele. (Gen 29:16-20, 23-25, 27-28)

5. Mulungu adampatsa Yakobo ana angati?
Ana aamuna 12 ndi wamkazi mmodzi. (Gen 35:22-26; onaninso Gen 30:21)

6. Kodi Labani adamsamalira bwino Yakobo?
Ayi; ankangosinthasintha malipiro ake. (Gen 29:24-25; 30:26-30; 31:7)

7. Zidatheka bwanji kuti Yakobo alemere?
Mulungu anali naye. (Gen 30:43; onaninso Gen 31:9-13)

8. Chifukwa chiyani Yakobo anasiyana ndi Labani?
Mulungu adamuuza kuti abwerere ku Kanani. (Gen 31:13)

9. Yakobo akubwerera ku Kanani, chinachitika nchiyani?
Analimbana ndi Mulungu. (Gen 32:24-26)

10. Kodi Esau adamupha Yakobo atabwerera kwawo?
Ayi, Mulungu adamletsa Esau kuti asamchitire Yakobo choyipa chirichonse. (Gen 33:4)

Vesi loloweza pamtima:
"Ndaonana ndi Mulungu nkhope ndi nkhope, ndipo wapulumuka moyo wanga." (Gen 32:30)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 14
YOSEFE
Genesesi 37, 39

1. Ndi mwana uti wa Yakobo amene ankamkondetsetsa?
Yosefe, mwana wa Rakele. (Gen 37:3)

2. Yakobo adawonetsa bwanji chikondi chake kwa Yakobo?
Anampatsa mwinjiro wa mitundu yosiyanasiyana. (Gen 37:3)

3. Chifukwa chiyani Yakobo anankonda Yosefe mwapadera?
Anafuna ampatse madalitso aukulu wake. (Gen 37:3)

4. Abale ake anamva nazo bwanji zimenezi?
Anachita nsanje ndi kudana naye. (Gen 37:4)

5. Chinapangitsa kuti adane naye koposa chinali chiyani?
Analota abale ake akumuwelamira. (Gen 37:5-11)

6. Abale ake anachita naye chiyani Yosefe?
Anamgulitsa ku ukapolo kwa a Eguputo. (Gen 37:20-28)

7. Abale a Yosefe adanamanji kwa atate awo atabwelera kwawo?
Chilombo cha kuthengo chidamudya Yosefe. (Gen 37:31-32)

8. Ku Eguputo, Yosefe anaona zotani?
Anamsankha kukhala wamkulu woyang'anira a mnyumba mwa Potifala. (Gen 39:1-4)

9. Potifala adamchita chiyani Yosefe?
Adamtsekera mndende. (Gen 39:20)

10. Yosefe adalakwitsa chilichonse?
Ayi; Mkazi wa Potifala adamunamizira. (Gen 39:7-18)

Vesi loloweza pamtima:
"Mikono ya manja ake inalimbitsidwa ndi manja a Wamphamvu wa Yakobo." (Gen 49:24)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 15
YOSEFE ALAMULIRA KU EGUPUTO
Genesesi 39-50

1. Mulungu adamtsogolera bwanji Yosefe pamene anali mndende?
Woyang'anira mndende ankamkonda kwambiri Yosefe. (Gen 39:21-23)

2. Yosefe adalowa mndende pamodzi ndi yani?
Wopereka chikho ndi wophika mkate wa mfumu. (Gen 40:1-3)

3. **Wopereka chikhoyu ndi wophika mkateyu anakwiya chifukwa chiyani tsiku lina?**
Mulungu anawalotetsa. (Gen 40:5-6)

4. Chinachitika nchiyani malotowa atawavutitsa?
Mulungu adamuonetsa Yosefe chomwe malotowa ankatanthauza. (Gen 40:8-19)

5. Wina ndani Mulungu adamulotetsa?
Farao, mfumu ya a Eguputo. (Gen 41:1)

6. Adatanthauzira maloto a mfumu ndani?
Yosefe, amene adamtulutsa mndende kuti akatanthauzire malotowo. (Gen 41:14-16)

7. Farao adamthokoza bwanji Yosefe?
Adamsankha kukhala wolamulira dziko lonse. (Gen 41:39-44)

8. Ndani adabwera kwa Yosefe?
Abale ake kudzagula zakudya. (Gen 42:1-6)

9. Kodi adamzindikira Yosefe?
Ayi, kufikira atawauza. (Gen 42:7-8; onaninso Gen 45:1-3)

10. Kodi Yakobo adakondwa atamva kuti mwana wake ali moyobe?
Inde, iye ndi ana ake adapita ndi kukakhazikika Eguputo. (Gen 45:28; 46:3-6, 26, 29-30)

Vesi loloweza pamtima:
"Koma inu munadipangira ine choipa; koma Mulungu anachipangira chabwino." (Gen 50:20)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 16
MOSE
Eksodo 2-4

1. Kodi a Israeli adakhala mosangalala ku Eguputo?
Ayi, kunabwera mfumu ina yankhanza yomwe inawayesa akapolo. (Eks 1:8-14)

2. Mfumu imeneyi idawalamulanji a Israeli?
Kutaya ana awo onse aamuna mumtsinje. (Eks 1:22)

3. Ndani adabadwa pa nthawiyi?
Mnyamata wokongola wotchedwa Mose. (Eks 2:2, 10)

4. Kodi makolo ake adamtaya mumtsinje?
Ayi, anamuika mbasiketi, nakaliika mumtsinje. (Eks 2:3)

5. Chifukwa chiyani mai ake a Mose anakasiya basiketilo kumtsinje?
Kuti mwana wamkazi wa mfumu ampezeko. (Eks 2:5-9)

6. Kodi mwana wa mfumu wamkaziyo anapita ndi mwanayo ku nyumba kwake?
Inde, koma anawalipira amai ake pamene anansamala mwanayo ali wamng'ono. (Eks 2:9-10)

7. Kodi Mose anafuna kukhalabe kwa mfumu?
Ayi, anafuna kuti akathandize anthu a Mulungu. (Eks 2:11-15; onaninso Ahe 11:24-25)

8. Mose anayesa bwanji kuthandiza anthu a Mulungu?
Anapha mu Eguputo ndi kuthawira ku Midiyani. (Eks 2:11-15)

9. Ndani adamuonekera Mose ku Midiyani?
Mulungu adamuonekera mchitsamba choyaka moto. (Eks 3:2-4)

10. Mulungu adamuuzanji Mose?
Abwerere ku Eguputo ndi kutsogolera a Israeli kutuluka mdzikolo. (Eks 3:7-10)

Vesi loloweza pamtima:
"Ndi chikhulupiliro, Mose atakula msinkhu, anakana kutchedwa mwana wake wa mwana wamkazi wa Farao." (Ahe 11:24)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 17
KUOMBOLEDWA KWA AISRAELI
Eksodo 5-14

1. Mose adamuuzanji Farao?
"Atero Yehova, Mulungu wa Israeli; lola anthu anga apite" (Eks 5:1)

2. Farao anachita chiyani pamene anamva lamuloli?
Farao anawazunzirazunzirabe. (Eks 5:2, 4-9)

3. Kodi Mulungu adawatumizira chiyani a Eguputo?
Mililí khumi yoopsa. (Eks 9:13-14)

4. Kodi mililiyi inagweranso a Israeli?
Ayi, Mulungu anawonetsetsa kuti awasamalire anthu ake. (Monga Eks 9:23-26)

5. Aisraeli anali kuchita chiyani pamene mulili wotsiriza udabwera?
Ankadya phwando la kutuluka. (Eks 12:21-30)

6. Mulili wotsiriza unali wotani?
Ana onse aamuna a Eguputo adafa. (Eks 12:29)

7. Kodi a Eguputo adakondwa poona a Israeli akupita?
Inde, mpaka kuwapatsa mphatso. (Eks 12:33, 35-36)

8. Kodi Farao adangowasiya a Israeli kuti apite mwantendere?
Ayi adawatsatira ndi ankhondo ake. (Eks 14:4-9)

9. Kodi Mulungu adapulumutsa a Israeli kwa Farao?
Inde, adawatsogolera kuwoloka Nyanja Yofiira pa malo ouma.
(Eks 14:13-14, 21-22, 29-30)

10. Farao anaona zotani?
Iye ndi ankhondo ake anamira mnyanja. (Eks 14:16-17, 23-28)

Vesi loloweza pamtima:
"Pamene ndiwona mwaziwo, ndidzapitilira inu." (Eks 12:13)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 18
AISRAELI MCHIPULULU

1. Kodi Mulungu adawalondolera bwanji aIsraele ku chipululu?
Ndi mtambo nthawi ya masana komanso moto nthawi ya usiku. (Eks 13:21-22)

2. Mulungu adawadyetsa bwanji a Israeli?
Adawatumizira mana ochokera kumwamba ndi madzi ochokera ku thanthwe. (Eks 16:13-15; 17:5-6)

3. Mulungu adaveka bwanji a Israeli mchipululu?
Zovala zawo ndi nsapato zawo sizinathe. (Deut 29:5)

4. Mulungu adawapatsa chiyani pa phiri la Sinai?
Malamulo. {Eks 24:12; onaninso Eks 20:1-17; Deut 5:6-21)

5. Kodi Mulungu adamuuza Mose kuti amange chiyani?
Kachisi mopemphereramo Mulungu. (Eks 25:1-9)

6. Aisraeli adachimwa potani ku Sinai?
Adapanga ndi kupembedza mwana wa ng'ombe wa golide. (Eks 32:19-24)

7. Ndi zoipa zina ziti zomwe adachita mchipululu?
Adalilira chakudya, komanso adaganiza kuti Mulungu sadzawapatsa madzi. (Num 20:1-5; 21:5)

8. Pamene aIsraeli adayandikira ku Kanani, Mose adachita chiyani?
Adatuma amuna 12 kukazonda dzikolo. (Num 13:1-20)

9. Kodi amuna onsewa adabweretsa uthenga wabwino?
Awiri okha ndiwo adatero koma ena onse adawachititsa anthu mantha. (Num 13:30-33; 14:6-9)

10. Aisraeli adachita chiyani atamva uthenga woipawo?
Adafuna kubwerera ku Eguputo. (Num 14:1-4)

Vesi loloweza pamtima:
"Yamikani Mulungu wakumwamba pakuti chifundo chake nchosatha." (Mas 136:26)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 19
AISRAELI MCHIPULULU (KUPITIRIZA)

1. **Mulungu adalanga bwanji a Israeli chifukwa chofuna kubwereranso ku Eguputo?**
   Aisraeli ankangoyendayenda mchipululu kwa zaka 40. (Num 14:20-34)

2. **Mulungu adalanga bwanji Kora, Datani ndi Abiramu?**
   Nthaka idatseguka ndi kuwameza. (Num 16:23-34)

3. **Aisraeli adaona zotani atatopa ndi kulimbirana mana?**
   Mulungu adawatumizira njoka zaululu zomwe zidapha anthu ambiri. (Num 21:5-6)

4. **Aisraeli adapulumuka bwanji kunjoka za ululuzo?**
   Ankayang'ana njoka ya mkuwa imene Mose adaipachika pamtengo. (Num 21:8-9)

5. **Ndani adafuna kuwononga Israeli?**
   Balaki, mfumu ya a Mowabu. (Num 22:1-4)

6. **Adafuna kuwononga bwanji Israeli?**
   Adauza mneneri wonama Balamu kuti atemberere Israeli. (Num 22:5-6)

7. **Balamu adatemberera Israeli?**
   Ayi, adadalitsa Israeli mmalo mwake. (Num 23:7-12, 15-19; 24:2-10)

8. **Israeli adawononga mafumu ati?**
   Ogi, mfumu ya Basana, ndi Sihoni, mfumu ya a Amori. (Num 21:23-24, 33-35)

9. **Kodi Mose adatsogolera a Israeli kupita ku Kanani?**
   Ayi, koma Mulungu adamuwonetsa dziko la Kanani kuchokera pa phiri la Nebo iye asanafe. (Deu 34:1-6)

10. **Chifukwa chiani Mose sanafike nawo ku Kanani?**
    Adamenya thanthwe ali wokwiya pomwe Mulungu adamuuza kuti angoliyankhula thanthwelo. (Num 20:12)

Vesi loloweza pamtima:
"Ndipo monga Mose anakweza njoka mchipululu, cotero mwana wa munthu ayenera kukwezedwa." (Yoh 3:14)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 20
ISRAELI ALOWA M'KANANI
Yoswa 1-10

1. Ndani adatsogolera Israeli Mose atafa?
Yoswa, mtumiki wa Mose. (Yos 1:1-2)

2. Kodi Yoswa adachita chiyani atayandikira Yeriko?
Adatuma anthu awiri okazonda mzinda. (Yos 2:1)

3. Israeli adaoloka bwanji Yorodani?
Mulungu adaumitsa mtsinjewo ndipo aIsraeli adawoloka pamalo ouma. (Yos 3:11-17)

4. Mulungu adawauza kuti akalande bwanji mzindawo?
Mulungu anawalamula kuti auzungulire linga la mzindawo masiku 7. (Yos 6:1-4, 15-16)

5. Adalowa bwanji mzinda wa Yeriko?
Mulungu adagwetsa linga la mzindawo. (Yos 6:5, 20)

6. Kodi Israeli adapha anthu onse a mYeriko?
Inde, kupatula Rahabu ndi banja lake chifukwa adabisa anthu okazonda aja. (Yos 6:21-25)

7. M'chifukwa chiyani Israeli sanagwire mzinda wa Ayi poyambirira?
Akani adaba zinthu ku Yeriko. (Yos 7:1, 10-11, 20-21)

8. Akani adalangidwa bwanji?
Iye ndi a m'banja mwake adaponyedwa miyala ndi kuotchedwa. (Yos 7:25)

9. Ndi njira yanji yapadera yomwe Mulungu adathandizira anthu ake kumenya nkhondo?
Adaimitsa dzuwa ndi mwezi. (Yos 10:12-13)

10. Chifukwa chiyani Mulungu adawapatsa dziko la Kanani?
Ngati chizindikiro cha dziko la kumwamba. (Onani Ahe 11:8-10, 13-16)

Vesi loloweza pamtima:
"Koma ine ndi a mnyumba mwanga, tidzatumikira Yehova." (Yos 24:15)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 21
EHUDI NDI DEBORA
Oweruza 3-5

1. Kodi a Israeli adatumikira Mulungu Yoswa atamwalira?
Ayi, adamuyiwala Mulungu ndikuyamba kupembedza mafano. (Owe 3:5-7)

2. Mulungu adalanga bwanji Israeli?
Mulungu adawapereka mmanja mwa adani awo. (Owe 3:8)

3. Kodi Mulungu adawathandiza?
Inde, adawapatsa mwayi woti alape, ndipo adatumiza oweruza kuti awathandize. (Owe 3:9-11)

4. Tchulani mfumu imodzi imene inadza ku Kanani kudzalamulira Israeli.
Egiloni mfumu ya a Mowabu. (Owe 3:12-14)

5. Israeli adaomboka bwanji kwa a Mowabu?
Ehudi, oweruza, anamupha Egiloni ndi lupanga. (Owe 3:15-26)

6. Anali oweruza ndani pamene a Kanani ankalamulira Israeli?
Debora, mneneri wamkazi. (Owe 4:2-4)

7. Debora adalamula ndani kuchita nkhondo ndi a Kanani?
Baraki, yemwe adakana kupita ku nkhondo ngati Debora sapita nawo. (Owe 4:6-9)

8. Kodi a Kanani anali ndi asilikali amphamvu?
Inde, analinso ndi akavalo ndi magareta. (Owe 4:13; 5:22)

9. Baraki adapambana bwanji nkhondo?
Mulungu adapatsa ankhondo ake mphamvu zomenyera nkhondo. (Owe 4:14-15; 5:12-23)

10. Kodi mtsogoleri wankhondo wa a Kanani, Sisera, adawona zotani?
Adaphedwa ndi mkazi pamene adabisala muhema mwake. (Owe 4:17-21; 5:24-27)

Vesi loloweza pamtima:
"Pamenepo adafuulira kwa Yehova mkusauka kwawo, ndipo awapulumutsa mkupsinjika kwawo." (Mas 107:19)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 22
GIDIYONI
Oweruza 6-8

1. **Amidiyani adalamulira Israeli kwa zaka zingati?**
   Zaka 7. (Owe 6:1)

2. **Adasowetsa Israeli bwanji mtendere?**
   Ankaba mbeu zawo. (Owe 6:2-6)

3. **Mulungu adauza Gidiyoni kuti achite chiyani?**
   Agwetse guwa lansembe la Bala, ndi kupereka nsembe kwa Mulungu (Owe 6:25-26)

4. **Gidiyoni adayamba bwanji kupulumutsa Israeli?**
   Adatuma ankhondo ambiri kukamenyana ndi aMidiyani. (Owe 6:34-35;7:3)

5. **Kodi Mulungu adafuna kuti Gidiyoni akhale ndi ankhondo ambiri?**
   Ayi, anafuna kuphunzitsa Israeli kuti Iye ndiye adzawapambanitsa. (Owe 7:2)

6. **Pomaliza Gidiyoni anatsala ndi ankhondo angati?**
   300. (Owe 7:4-7)

7. **Gidiyoni adakonzekera bwanji asirikali ake?**
   Msilikali aliyense anali ndi lipenga ndi nyali mkati mwa mbiya. (Owe 7:15-16)

8. **Ankhondo a Gidiyoni adachita nawo chiyani malipenga ndi mbiya zija?**
   Adayimba malipengawo ndi mbiyazo. (Owe 7:19-20)

9. **Ankhondo a Gidiyoni ankakuwa kuti chiyani popita ku nkhondo?**
   "Lupanga la Yehova ndi Gidiyoni" (Owe 7:18)

10. **AMidiyani adawona zotani?**
    Adawathamangitsa mdzikolo. (Owe 8:28)

Vesi loloweza pamtima:
"Auke Mulungu, abalalike adani ake." (Mas 68:1)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 23
SAMSONI
Oweruza 13-16

1. **Mulungu adaitana ndani kuti athire nkhondo a Filisti?**
   Samsoni. (Owe 13:24-25, onaninso v 5)

2. **Mngelo adawauzanji makolo a Samsoni za iye?**
   Adzakhala mNazareti. (Owe 13:3-5)

3. **Zinatheka bwanji Samsoni kumenya nkhondo yekha?**
   Mzimu wa Yehova unampatsa mphamvu zambiri. (Owe 14:5-6, 19; 15:14-15)

4. **Chifukwa ninji Samsoni anagwira nkhandwe 300?**
   Kuti aotche tirigu mminda ya a Filisti. (Owe 15:4-5)

5. **Chibwano cha buru adachita nacho chiyani?**
   Adaphera a Filisti 1000. (Owe 15:14-15)

6. **Zipata za mmudzi, Samsoni adachita nazo chiyani?**
   Adapita nazo pa phiri lalitali. (Owe 16:2-3)

7. **Samson adachimwanji?**
   Adakwatira mkazi wachikunja. (Owe 16:4)

8. **Adawona zotani tsitsi lake atalimeta?**
   Mphamvu zake zonse zidamchokera. (Owe 16:17-19)

9. **Zitamchokera mphamvu a Filisti anamtani?**
   Anankolowola maso ndi kumponya mndende. (Owe 16:21)

10. **Kodi Mulungu adamva pemphero la Samsoni?**
    Inde, komanso a Filisti ambiri anafa pamene nyumba ya Dagoni inagwa. (Owe 16:26-30)

Vesi loloweza pamtima:
"Yehova ndiye kuunika kwanga ndi chipulumutso changa; ndidzaopa yani?" (Mas 27:1)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 24
RUTE
Buku la Rute

1. Chifukwa chiyani Naomi anapita ku Mowabu?
Ku Israeli kunali njala yaikulu. (Rut 1:1)

2. Ana ake awiri a amuna anachita chiyani?
Anakwatira akazi a ku Mowabu. (Rut 1:2-4)

3. Kodi Mulungu anadalitsa banja la Naomi ku Mowabu?
Ayi, mwamuna wake ndi ana ake aamuna awiri anamwalira. (Rut 1:3, 5, onaninso v 20-21)

4. Naomi anaphunzira chiyani pa imfayi?
Anayenera kubwerera ku Israeli kuti akalandire madalitso a Mulungu. (Rut 1:6)

5. Kodi Rute ndi Olipa onse anapitila limodzi ndi Naomi?
Ayi, Rute yekha ndiye anapita nawo. (Rut 1:7-14)

6. Chifukwa chiyani Rute anapita nawo?
Ankakonda Mulungu. (Rut 1:16-17; 2:12)

7. Rute anati chiyani?
Anthu akwanu ndiwo anthu a kwa inenso, ndi Mulungu wanu ndiye Mulungu wanga" (Rut 1:16)

8. Rute anamdziwa bwanji Bowazi?
Rute ankakhunkha tirigu mmunda mwa Bowazi. (Rut 2:1-3)

9. Bowazi anamchitira chiyani Rute?
Anamteteza ndi kumchitira chifundo. (Rut 2:8-9, 14-16)

10. Kodi Rute anakwatiwa ndi Bowazi
Inde, ndipo anakhala kholo la Davide. (Rut 4:10, 13-17)

Vesi loloweza pamtima:
"Musandiumirize kuti ndikusiyeni, ndikubwerera osakutsatani." (Rut 1:16)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 25
SAMUELI
1 Samueli 1-9

1. Kodi Hana anapempha chiyani kwa Mulungu?
Mwana amene adzatumikira Yehova. (1 Sam 1:10-11, 15)

2. Kodi Yehova adamva pemphero lake?
Inde, adampatsa Samueli. (1 Sam 1:19-20)

3. Mayi ake a Samueli adapita naye kuti?
Kwa Eli, wansembe, kuti akatumikire ku Nyumba ya Mulungu. (1 Sam 1:24-28)

4. Samueli adaona zotani akali wamng'ono?
Yehova adamuitana ndi kulankhula naye. (1 Sam 3:2-10)

5. Yehova adamuuza chiyani Samueli?
Eli ndi ana ake woipa adzafa onse tsiku limodzi. (1 Sam 3:11-14)

6. Ana a Eli anafa bwanji?
Anafera ku nkhondo ndi a Filisti. (1 Sam 4:11, 16-17)

7. Pankhondo imeneyi kunachitikanso zotani?
Likasa la Chipangano linatengedwa. (1 Sam 4:11, 17)

8. Eli anaona zotani atamva kuti Bokosi la Chipangano latengedwa?
Anagwa pampando wake ndi kuthyola khosi. (1 Sam 4:18)

9. Chifukwa chiyani aFilisti analibweza Bokosi la Chipangano ku Israeli?
Mulungu adawatumizira miliri. (1 Sam 5:1-6:2, 7-15)

10. Anthu adampempha chiyani Samueli?
Awapatse mfumu. (1 Sam 8:5-22)

V*esi loloweza pamtima:* "Pompo Samueli anayankha, Nenani, popeza mnyamata wanu alikumva." (1 Sam 3:10)

Copyright © Gratia Dei Sola Media